

# Analimba Mtima Pochita Zinthu Zabwino

**Malangizo:** Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwa, yerekezani kuti inuyo mukuona pamene nkhaniyo ikuchitika. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a m'nkhaniyi akumvera mumtima mwawo.

**Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi:** Baruki, Yeremiya ndiponso akalonga a ku Yuda

**Chidule cha nkhaniyi:** Baruki analemba mawu amene Yeremiya anamuza ndipo anawawerenga mokweza kwa akalonga a ku Yuda.

1

## GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI YEREMIYA 36:4-32.

Kodi mukuganiza kuti 'chipinda chodyera cha mlembi, kumene akalonga onse anali atakhala panso' chinkaoneka bwanji?

---



---

Kodi mukuganiza kuti Baruki ankamva bwanji pamene ankawerenga mokweza mawu a Yeremiya kwa akalongawo?

---



---

Kodi mukuganiza kuti akalonga ankamva bwanji mumtima mwawo pamene ankauza Baruki mawu omwe ali pavesi 16 mpaka 19?

---



---

2

## FUFUZANI MOZAMA.

Kodi mukuganiza kuti zinali zophweka kuti Baruki alembe mawu a Yeremiya “mumpukutu” kawiri konse? (Zokuthandizani: **Werenganinso Yeremiya 36:4, 32.**)

---



---

N'chifukwa chiyani mwina sizinali zophweka kuti Baruki alembe ulosi wa Yeremiya ndiponso kuuwerenga mokweza? (Werengani Yeremiya 26:8.)

---



---

Yeremiya anali atalosera kwa anthuwo kwa zaka zambiri. Nanga n'chifukwa chiyani iye ankafuna kuti Baruki awerenge ulosiwo mokweza? (Zokuthandizani: **Werenganinso Yeremiya 36:7.**)

---



---

3

### GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .

Chifukwa chimene anthu a Mulungu amafunika kukhala olimba mtima.

---



---

Mmene Yehova Mulungu amadalitsira anthu amene amalimba mtima pochita zinthu zabwino.

---



---

4

### DZIFUNSENI KUTI:

Kodi ndimafunika kulimba mtima ndikamakumana ndi zinthu ziti?

---



---

Kodi ndikamachita manyazi kapena mantha, ndingatani kuti ndilimba mtima? (Werengani Afilipi 4:6, 7.)

---



---

M'nkhaniyi, kodi ndi mfundo iti imene yandikhudza mtima kwambiri, ndipo n'chifukwa chiyani?

---



---




---



---

**Mungachite izi:** Yerekezani kuti ndinu mtolankhani ndipo mukupereka lipoti la nkhaniyi pa wailesi kapena pa TV. Fotokozani zimene zinachitika ndipo mufunse mafunso anthu amene akutchulidwa m'nkhaniyi komanso amene anaona pamene zinthuzo zinkachitika.



Koperani ndi kusindikiza nkhaniyi pa [www.jw.org](http://www.jw.org)